
***Kodi cholinga cha kafukufuku wa HOPE ndi chiyani?*** Cholinga choyambirira cha kafukufuku wa HOPE ndi kufuna kupereka mwayi koyamba kwa olowa kafukufuku opeza ling'i yovalira munjira ya abambo yomwe inapezeka kuti ndi njira ina yodzitetezera ku HIV. Tikufuna timvetsetse kuti ndi chifukwa chiyani olowa kafukufuku angasankhe kapena kusasankha ling'i ngati njira yodzitetezera ku HIV, ndiponso ngati chisankho chitha kusintha pakapita nthawi.

| **Kodi kafukufuku wa HOPE ndi osiyana bwanji ndi kafukufuku wa ASPIRE** | |
|---|---|
| **ASPIRE** | **HOPE** |
| Cholinga: Kutsimikizira ngati ling'i inalidi yosaopsya kuigwiritsa ntchito komanso kuti ndiyogwira ntchito poteteza kutengera HIV. | Cholinga: Kumvetsetsa ngati amai adzagwiritse ntchito ling'i, ngati atapatsidwa mwayi umenewo. |
| Anayeza ngati ling'i inali yosaopsya kuigwiritsa ntchito | Tikudziwa kuti ling'i ndi yosaopsya ndithu |
| Anayeza ngati ling'i ingathandize kupewa matenda a HIV | Tikudziwa kuti ling'i imeneyi itha kuchepetsa mpata otengera matenda a HIV kwa azimai |
| Theka la amai linalandira ling'i yokhala ndi mankhwala omwe amayesedwa ndipo theka linalo linalandira ling'i yopanda mankhwalawa | Ma ling'i onse ali ndi mankhwala omwe akufufuzidwa |
| Otenga nawo mbali mukafukufuku onse anayenera kuvomereza kugwiritsa ntchito ling'i | Kugwiritsa ntchito ling'i ndi chisankho cha olowa kafukufuku aliyense payekha! |
| … | … |

***Ndiye mukunena kuti amai atha kusankha kugwiritsa ntchito chibangiri(ling'i) mukafukufuku wa HOPE?*** Inde. Amai atha kulowa kafukufuku ndikusankha kugwiritsa ntchito kapena kusagwiritsa ntchito ling'i imeneyi ngati chida chozitetezera. Onse olowa kafukufuku adzalandira phindu lofanana chifukwa chokhala mukafukufukuyu, posatengera chisankho chawo pankhani yogwiritsa ntchito ling'i. Chifukwa olowa kafukufuku ali ndi mwayi osankha, tikupempha kuti iwo adzatenge ling'i pokhapokha ngati akufuna kukaigwiritsa ntchito. Olowa kafukufuku atha kusintha maganizo awo nthawi iliyonse pankhani yogwiritsa ntchito ling'i pamene kafukufuku akuchitika.



***Pakuti kafukufuku wa ASPIRE anawonetsa kuti ling'i ndi yosaopsya kuigwirtsa ntchito ndipo ndi yogwira ntchito, ndi chifukwa chiyani mukupereka mpata kwa olowa kafukufuku wa HOPE kuti atha kusankha kusaigwiritsa ntchito?*** Kafukufuku wa HOPE akufuna kumvetsetsa ngati amai atha kuigwiritsa ntchito komanso kuti angaigwiritse bwanji ntchito ling'i maka pamene zadziwika kuti ndi yosaopsa ndipo ndi yogwira ntchito. Tikudziwa ma kondomu ndi osaopsya ndipo amagwira ntchito, koma anthu ambiri amasankha kusawagwiritsa ntchito komanso kuona chovuta kuwagwiritsa ntchito. Timamvetsetsa chifukwa chomwe anthu amagwiritsira kapena kusagwiritsa ntchito makondomu ndipo tikufuna tipeze zinthu ngati zimenezo komano zokhudza ling'i. Olowa kafukufuku ena atha kusankha kusagwiritsa ntchito ling'i, komabe atha kuthandiza popereka maganizo awo maka pa zovuta zogwiritsa ntchito ling'i kapena kuti ndi chani sichiwasangalatsa. Zofuna kuzitetera ku HIV komanso zokonda za otenga nawo mbali zingathenso kusintha nthawi iliyonse.

**Makamaka, tikufuna kuti mai aliyense amvetsetse za chiopsyezo chotengera HIV chomwe ali nacho, njira zonse zopewera HIV zomwe atha kuzipeza, ndi kusankhapo njira zomwe akuona kuti zitha kumuthandiza pa moyo wake.**

Ogwira ntchito kukafukufuku wa HOPE ndi amene amagwira ntchito yophunzitsa anthu za akafukufuku atha kugwira ntchito limodzi ndi olowa kafukufuku pakumuthandiza kuti azindikire ndi kumvetsetsa chiopsyezo chotengera HIV chomwe ali nacho. Tikufuna amai akhale omasuka kusankha kugwiritsa ntchito ling'i kapena ayi, ndi kusintha maganizo awo, popanda kuweruzidwa ndi ogwira ntchito kukafukufuku kapena wina olowa kafukufuku.

**Ndi zoona kuti amai omwe alowe kafukufuku wa HOPE koma sakugwiritsa ntchito ling'i akhala akuthandiza ndi china chake mukafukufukuyu?**
Onse olowa kafukufuku wa HOPE akhala akuthandiza kupereka uthenga ofunikira kwambiri mukafukufukuyu, kaya asankha kugwiritsa ntchito ling'i kapena ayi. Zomwe adzanene onse olowa kafukufuku zidzathandiza kupititsa patsogolo kamvetsetsedwe kathu ka ling'i imeneyi ndi mmene tingathandizire amai pa kagwiritsidwe ntchito ka ling'i mtsogolo.



Ngati muli ndi mafunso kapena mukufuna uthenga wochulukirapo, chonde pitani ku kiliniki ya kafukufuku:

Version 1.0, CHICHEWA, 16NOV2016

HOPE

Out of ASPIRE, there is HOPE

# CHISANKHO MU KAFUKUFUKU WA HOPE

